Mudzina la Allah, Wachifundo chambiri, Wachisoni chosatha

Kuloleza Zinthu Zoletsedwa

ZIDA ZA NYIMBO

(Kuimba ndi Kumvera Nyimbo)

Kuzikongoletsa zinthu za haram nkuzisandutsa kukhala za halaal popanda umboni kuchokera mu Qur'an ndi Sunnah:

Abu Turaab Adhwaahiri analemba *article* mu *magazine* yotchedwa Al-Raaid kuti: "Qur'an ndi Sunnah sizinaletse nyimbo, komanso sizinaletse kugwiritsa ntchito zida zanyimbo ngakhale kumvera".

Analongosola izi pogwiritsa ntchito ma Hadith komanso nkhani zina zopeka, zololeza nyimbo potsatira imam wake Abu Muhammad ibn Hazm Adhwaahiri. Komanso anagwiritsa ntchito zoyankhula za imam wake Abu Muhammad Ali yemwe anawapanga ma Hadith onse omwe akuletsa nyimbozi kuti ndi ofooka, ndipo sanasiyire pomwepo koma anatsindika polankhula monyoza kuti ma Hadith amenewo ndi opeka.

Ma aayah komanso ma Hadith ambiri omwe ndi owona opanda chikaiko chirichonse alongosola za kuletsedwa kwa zida za nyimbo, koma ma imam amenewa anakanira, ndipo anawalimbikitsa anthu kutsutsa ma Aayah ndi ma Hadith amenewa.

Ndikupempha chikhululuko cha Allah Ta'ala komanso madalitso ake, pakuyankhula zabwino ndi kupewa kuyankhula zopanda nazo kuzindikira kulikonse, ndipo atitalikitse ku kupanga halaal za haraam popanda umboni wochokera kwa iye ndi Mtumiki wake.

Ma 'Ulamaa odalirika anatsutsa kale zoyankhula za imam ameneyu ndipo anachenjeza za kutenga zoyankhula zake zonse, chifukwa zambiri mwa izo zinasokoneza Ummah ndipo ena mwa otsatira zimenezo ndiomwe akuchita makani panthawi ino potsutsana ndi ma Aayah ndi ma Hadith oletsa nyimbo. Fitna inakwanira pakati pathu chifukwa cha ma Sheikh osocheretsa, omwe amati akayankhula kapena kulemba mma *social media*'mu ena nkunena kuti nzolakwika, anthu ena amafunsa mafunso ngati awa: "kodi sheikhwo sankadziwa koma inu? Kodi inuyo ndiye ophunzira kuposa sheikhwo?"

Konseko kumakhala kusapota bodza lomwe akulalikiralo, komanso kukomedwa ndi zinthu za haraam zomwe sheikhwo akuzipanga kukhala za halaal. Allah atiteteze ku fitna imeneyi.

Allah Ta’ala anachenjeza za kumuyankhulira zinthu zomwe tilibe nazo kuzindikira komanso anatiletsa kuloleza ndi kulesa zinthu popanda umboni. Iye (Allah Ta’ala) anatichenjeza kuti imeneyo ndi ntchito ya shaytwaan yemwe amanka nakongoletsa zoipa pakati pa anthu:

﴿ قُلْ إِنَّمَا حَرَّمَ رَبِّيَ ٱلْفَوَٰحِشَ مَا ظَهَرَ مِنْهَا وَمَا بَطَنَ وَٱلْإِثْمَ وَٱلْبَغْيَ بِغَيْرِ ٱلْحَقِّ وَأَن تُشْرِكُوا۟ بِٱللَّهِ مَا لَمْ يُنَزِّلْ بِهِۦ سُلْطَٰنًا وَأَن تَقُولُوا۟ عَلَى ٱللَّهِ مَا لَا تَعْلَمُونَ ﴿٣٣﴾ ﴾

“Nena (kwa iwo): “Ndithu Mbuye wanga waletsa zinthu zauve zoonekera ndi zobisika, ndi machimo, ndi kuwukira (atsogoleri) popanda choonadi, ndi kumphatikiza Allah ndi chomwe sadachitsitsire umboni (wakuti chiphatikizidwe ndi Iye); ndiponso (waletsa) kumunenera Allah zimene simukuzidziwa.”[1]

Allah Ta'ala ananenanso kuti:

﴿ وَلَا تَقُولُوا۟ لِمَا تَصِفُ أَلْسِنَتُكُمُ ٱلْكَذِبَ هَٰذَا حَلَٰلٌ وَهَٰذَا حَرَامٌ لِّتَفْتَرُوا۟ عَلَى ٱللَّهِ ٱلْكَذِبَ ۚ إِنَّ ٱلَّذِينَ يَفْتَرُونَ عَلَى ٱللَّهِ ٱلْكَذِبَ لَا يُفْلِحُونَ ﴿١١٦﴾ مَتَٰعٌ قَلِيلٌ وَلَهُمْ عَذَابٌ أَلِيمٌ ﴿١١٧﴾ ﴾

“Ndipo musanene chifukwa chabodza lomwe malirime anu akunena (kuti) “Ichi nchololedwa; ichi ncholetsedwa (popanda umboni).” Kuopera kuti mungampekere bodza Allah. Ndithu, amene akupekera bodza Allah, sangapambane. Ndichisangalalo chochepa (cha m’dziko lapansi chimene chikuwachititsa zimenezo); ndipo iwo adzapata chilango chowawa.”[2]

Komanso anati:

﴿ يَٰٓأَيُّهَا ٱلنَّاسُ كُلُوا۟ مِمَّا فِى ٱلْأَرْضِ حَلَٰلًا طَيِّبًا وَلَا تَتَّبِعُوا۟ خُطُوَٰتِ ٱلشَّيْطَٰنِ ۚ إِنَّهُۥ لَكُمْ عَدُوٌّ مُّبِينٌ ﴿١٦٨﴾ إِنَّمَا يَأْمُرُكُم بِٱلسُّوٓءِ وَٱلْفَحْشَآءِ وَأَن تَقُولُوا۟ عَلَى ٱللَّهِ مَا لَا تَعْلَمُونَ ﴿١٦٩﴾ ﴾

“E inu anthu! Idyani zabwino zimene zili m’nthaka zomwe zili zololedwa; Ndipo musatsate mapazi a satana. Iye kwa inu ndi mdani woonekeratu. Iye

[1] Surah Al-A'raaf 33
[2] Surah Al-Nahl 116-117

akukulamulani kuchita zinthu zoipa ndi zauve. Ndikuti mumnamizire Allah pomunenera zimene simukuzidziwa."[3]

Allah Ta'ala akuchenjeza akapolo ake mma Aayah amenewo pa zakuloleza zinthu zomwe Iye analetsa kapena kuletsa zomwe Iye analoleza, mopanda kuzindikira. Ndipo Allah walongosola kuti kuyankhula kopanda nako 'ilm ndikoopsa. Allah anachenjeza akapolo ake kuti shaytwaan amawakonda pamene akuyankhula zokhudza Allah mopanda kuzindikira, ndipo amawalamulira kutero nthawi zonse mchipembedzo, mmakhalidwe komanso mmisonkhano yawo.

Zomwe zili zofunika kwa Msilamu aliyense ndiye kupewa kuyankhula zokhudza deen pomwe alibe 'ilm pazinthuzo, komanso azimuopa Allah ndikuwonetsetsa kuti zomwe akuzitchula kuti ndi haraam kapena halaal zizichokera mu Qur'an kapena Sunnah. Osangoti izi haraam, iziz halaal.

Msilamu aliyense apewe kutsatira ma imam osocheretsa, apewe kutsatira zoyankhula mu deen zopanda nazo umboni.

Msilamu yemwe ali wozindikira (wophunzira za Deen), asabise 'ilm chifukwa cha kuopa kuti awasokoneza anthu, chifukwa zomwe akubisazo, kusazidziwa kwa anthu nkomwe kukupangitsa kuti Chipembedzo chizisokonekera. 'Aalim asawasiye anthu mu umbuli chifukwa choti zomwe akuyenera kuwalongosolerazo n'zachilendo kwa iwo, koma alongosole deen kuti zaumbuli zomwe anazolowera anthuzo asiye. Osawasiyira anthu shirk chifukwa choti anazolowera. Osaopa kuwaphunzitsa anthu haqq chifukwa choti sanazolowere.

Ndikupempha Allah Ta'ala apereke chilimbikitso kwa ma 'Ulamaa athu ndi ma Sheikh onse, komanso apereke kugonjera mmitima mwa onse omwe akuphunzira deen.

[3] Surah Al Baqarah 168-169